


ZIKUMBUTSO ZOYESEDWA

NDI NTHAWI ZA MULUNGU

 Ndipo kungozizunguritsa izo mozungulira, kudutsa mu Baibulo, momwe ife...inu mwatengera Bukhu la Chivumbulutso, ndi Bukhu la Eksodo ndi Genesis. Ndipo tsopano ndabwera kwathu kuti ndipite kukasaka agologolo. Ndi kuwonamtima. Ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo, kungokhala woonamtima. Ndipo, M'bale Roy, inu mupita liti? [M'bale Roy akuti, "Mawa."—Mkonzi]. Mawa. Chabwino. Chotero ife timangokonda kubwera kwathu nthawi ino ya chaka, chotero, ndizo, ife tikufuna kuti tidzapume.

² Ine ndataya mapaundi twente kuchokera pamene ine ndinakuwonani inu. Ine ndinakwera pa sikelo, pamene ine ndinachoka ku msonkhano uwu, ine ndimalemera handiredi sikisite-faivi; ndipo nditabwerera, ndikulemera handiredi ndi forte-faivi. Chotero, ndikumverera ngati zovala zanga zikundikhwepa. Chotero, ine ndataya thupi kwambiri.

³ Ndipo dona wina, lero, akutuluka, mlongo wokonedwa, iye anati, "M'bale Branham, mupemphere kuti ine ndikhoze kutaya ilo, inenso."

⁴ Ndipo iye ndi wamphamvu, chotero ine ndinamuza iye, "Ingobwerani, tipite limodzi, muzikalalikira mwamphamvu kwambiri." Chotero, ndizo zonse zimene ine ndimazidziwa, izo ndithudi zidzalitsitsira ilo pansi. Koma, posachedwapa ife tidzathana nawo mavuto ndi mayesero.

⁵ Ndimaganiza za kukalamba. Inu mukudziwa, zaka zina ziwiri, ine ndikhala ndiri fifite. Psyii! Ine ndikukumbukira pamene Frankie Weber anakwanitsa. Iye ndi wamkulu pafupifupi zaka ziwiri kundiposa ine. Iye anakwanitsa kotala kukhala chopereka chake cha tsiku lakubadwa, kuno. Ndipo ine ndinaphethira diso langa, ndipo ine ndinaganiza, "Mai, Frankie Weber, usinkhu wa zaka twente-faivi, kotala ya handiredi!" Ndi theka tsopano. Basi sizimatenga nthawi yayitali, si choncho? Zimangopitirirabe.

⁶ Ife sitikhala nthawi yaitali. Basi m'mawa uno, pamene m'bale wathu wokonedwa anali kubweretsa uthenga wochititsa chidwi kwambiri umenewo, ine ndikutsimikiza kuti tonse tinasangalala nawo. Ndipo ndinapezeka ndikuganiza za chinachake pamene iye anali kulalikira, kumbuyo uko, ndipo ine ndinaganiza, "Mwinamwake Ambuye akhoza kundipatsa ine Lemba la zimenezo." Ine ndinamupangitsa iye kuti awerenge ena usikuuno kuchokera mu Mawu odalitsidwa a Mulungu. Ndipo

tsopano ine. . . maminiti pang'ono chabe kuti ndiyankhulepo, ndipo kenako ife tipempherera odwala, monga mwachizolowezi.

⁷ Ndipo Lachitatu usiku, Lachitatu likubwerali usiku, ngati Ambuye adzalola, ine ndikufuna kuti ndidzayambe mu Bukhu la Ahebri, ngati ziri bwino. Ndipo Bukhu la Ahebri, kwa phunziro. Ndipo kenako, mwinamwake, Lamlungu mmawa kapena Lamlungu usiku, kudzazipitiriza izo. Ndiye Lachitatu lotsatira usiku, mwinamwake kudzazitenganso izo kachiwiri, basi kumangopitirira kumazizunguza izo, mu Lemba.

⁸ Ndipo pali zinthu zina zimene ine ndinaziwona mu mpingo, basi pamene ine ndimadutsa, zimene ine ndikuganiza ziyenera kuphunzitsidwa pang'ono, inu mukudziwa, zinthu zomwe zimawoneka zofooketsa pang'ono. Ndipo ine ndikuganiza ife tikhoza kuzitenga izo mu Ahebri. Ndi a—ndi mutu wabwino kwambiri, malo abwino kuwawerenga. Tsopano, M'bale Neville. . . Ine ndinali kupita. . . Izo zinabwera mmalingaliro anga, ndikubwera kuno.

⁹ Ndipo ine ndangokhala ndi Chipangano Chatsopano pano, ndipo ine ndikuwerenga kuchokera mu Baibulo la Collins, zilembo zake ndi zazikulu. Ine nda. . . Pamene ndafika pafupifupi fifite, ine ndimayenera ndizilikankhira ilo kutali kwambiri ndi ine, kuti ndiwerenge zilembo zazing'ono kwenikweni zimenezo; ndi kuwala kosakwanira, mulimonse. Ndipo ine ndimapita kunja mu kuwala kwa dzuwa ndi kukawerengabe izo. Koma pamene kuwala kukakhala kochepera pang'ono, ine ndimayenera ndilikankhire ilo kutali. Ndipo adokotala anandiuza ine kuti posachedwapa ndikhala ndi magalasi owerengera.

Ndipo ine ndinamufunsa iye, “Maso anga ayipa?”

¹⁰ Ndipo iye anawayesa iwo. Anati, “Ayi. Teni-teni, ndiye kuti ali bwino kwambiri. Twente-twente ndiye kuti alibwino, ndipo—ndipo fifitini-fifitini ndiye kuti ndi abwinoko.” Ndipo teni-teni, ndi, ndizo zonse zimene iye anakhoza kuwerenga izo. Chotero ndimakhocha kuwerenga paliponse pamene iye amafuna, cha patali. Iye anatulutsa chinachake, ndipo ndinayamba kuwerenga izo. Pamene iye amafika pafupi, ine ndimayamba kuchedwera chedwera. Ine ndinadzaima pamene izo zimangofika monga *chonchi*. Iye anati, “Oh, eya, iwe wadutsa forte.”

Ndipo ine ndinati, “Eya.”

¹¹ Iye anati, “Chabwino, mwachirengedwe, mipira ya mdiso lako imaphwa.” Anati, “Tsopano, ngati mutamakhala moyo wabwino, wautali, inu mudzakhala nako kupenya kwachiwiri, ine ndikuyembekeza. Ndi pamene inu mungadzathe kumawerenganso kachiwiri.”

¹² Koma, inu mukudziwa, ine ndimangoganiza, izo siziri patali kwambiri, pamenepo. Kanthawi pang'ono chabe. M'bale Tony, izo nzoipa, sichoncho izo? [M'bale Tony akuti, “Ayi.”—Mkonzi].

Ayi, izo sichoncho. Ndi chinthu chodala. Ine ndikukalamba, mwanjira ina, ndi wocheperapo kenanso, chifukwa ine ndikupita kukhala wachinyamata ameneyo, wachisavundi, thupi lodalitsika, kumene, m'bale, sikudzakhala kalikonse kolakwika Kumeneko. Ndipo ine ndikungokhalira moyo nthawi imeneyo. Izo zidzakhala zodabwitsa.

¹³ Tsopano, ine ndisanawerenge mutu wotsekera wotsiriza, mawu chabe kwa Iye pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

¹⁴ Ife tikukhulupirira, Mulungu Wamphamvuzonse, kuti Inu mukufuna kuti ana Anu akhale osangalala. Izo sizinakonzedwe kuti ife tizikhala amatsinya ndi achisoni, pakuti kunalembedwa, kuti, "Mtima wokondwera umachita bwino ngati mankhwala." Ndipo ife timakonda kusangalala ndi madalitso Anu ndi kukhala nacho chiyanjano chachikulu ichi pamodzi. Ndipo monga ife . . .

¹⁵ Monga okhulupirira mu Mawu Anu, ife timayanjana mozungulira Mawu. Ndicho chimene ife tadzera pano, sikuti tidzangomvetsera Uthenga, koma kudzapembedza ndi kudzayanjana ndi Inu, kudzera mu kuwerenga ndi kulalikira kwa Mawu. Tsopano, Ambuye, Inu simudzatikhumudwitsa ife. Ine ndikutsimikiza Inu mutidalitsa ife mu maora awa.

¹⁶ Mdalitseni m'busa wathu wolemekezeka ndi wabwino, Ambuye. Ife tikupemphera kuti Inu mukhale naye iye. Ndipo monga ine ndinamuzindikira iye lero, mu kulalikira kwake, ndi kumuwona iye pamene amamwetulira pamene iye amayimba nyimbo ija, "Posachedwa ine ndidzathana nawo mavuto ndi mayesero." Ndi alongo amenewo, ndi momwe iwo amaimbira iyo akuzungulira mu tchire ndi mmisonkhano ya msasa. Ndipo izo zidzachitidwa, limodzi la masiku awa, ndipo kenako tizidzapita ku Mpumulo waulemelero umenewo.

¹⁷ Tsopano, Atate, tidalitseni ife pamene ife tikuwerenga Mawu Anu, ndi kuwawerenga Iwo, ndi kutsitsimutsa malingaliro athu ndi mitima. Ndipo yankhulani ndi ife, usikuuno. Ndipo pamene msonkhano ukatha, ndipo tikawuyamba wopita kwathu, mulole ife tikanene, "Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu pamene Iye amayankhula nafe pa njira?" Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁸ Tsopano ndi uthenga wabwino weniweni woterowo wa uvangeli monga ife tinali nawo mmawa uno, ndipo ine ndimaganiza, kuti, inu mukudziwa, M'bale Neville amayankhula za kudyetisa ana mopitirira muyezo. Chimene, inu mukhoza. Koma tsopano, usikuuno, ife tingokhala ndi kuyankhula pang'ono kwa mpingo. Uku ndi kuyankhulana chabe ndi mpingo. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge a . . . gawo lina la Lemba, mu Chipangano Chatsopano, Mateyu mutu wa 24, ndi ndime ya 35, Yesu akuyankhula.

Miyamba *ndi dziko lapansi zidzapita, koma mawu anga sadzapita.*

¹⁹ Phunziro langa usikuuno ndi—zikumbutso: *Zikumbutso Zoyesedwa Ndi Nthawi Za Mulungu.*

²⁰ Ndipo ine ndiri ndi zolengeza zingapo. Ine ndikukhulupirira ine ndinapanga izo, kwa . . . ndi ena apa kuti . . . za msonkhano woyamba ndi Ahebri, mutu wa 1, Lachitatu usiku, ngati Ambuye alola. Chifukwa chimene ine ndimayenera kuzitchula izo, kuti, monga, misonkhano yanga, ine ndikhoza kukhala pa malo amodzi, ndipo Iye amandiitanira ine wina. Ine ndimangoyenera kuti ndizipita pamene Iye akundiitana, inu mukudziwa.

²¹ Ndi chifukwa chake ine sindingakhale monga M'bale Oral Roberts ndi anthu amenewo amene amaika misonkhano yawo zaka ziwiri kapena zitatu mtsogolo, ndipo, "Ife tidzakhala kumeneko," ndi amuna aakulu achikhulupiriro champhamvu amenewo. Iwo—iwo—iwo ali ndi uthenga wawo.

²² Koma Uthenga wanga umangokhala kulikonse kumene Mulungu andituma, kaya ndi kuno, uko, kulikonse kumene kungakhale. Ine ndimayenera kuti ndizipita basi pamene Iye andituma. Ndipo ndi mautumiki awiri osiyana; kokha, Mulungu yemweyo, Mulungu yemwe yemweyo.

²³ Ine ndimaganiza, dzulo, mukuyankhula kwanga kwa mnyamata woyandikana naye wanga. Ndipo iye anati, "Inu mukudziwa, m'busa wina wamng'ono," iye anati, "iye ndi munthu wodabwitsa kwambiri." Anati, "Mkazanga ndi ine tinali titakhala titavala zovala zathu zogonera," ndipo anati, "pafupifupi leveni koloko usiku, ndipo iye anabwera ndipo anadzagogoda pakhomo. Anati, 'Ine ndangobwera modutsira kudzamwa nanu khofi.'" Mukuona? Ndipo anati, "Iye anawoloka msewu, kupita kwa woyandikana naye wina, ndipo iwo anali atakonzeka kuti azipita kokagona, ndipo iye anakadya keke kumeneko. Ndipo basi . . ." Ndipo kenako iye anati, "Iye ndi—iye anali ndi sukulu yaing'ono ya Baibulo ya ana, ndipo iye anali ndi ana aang'ono ochuluka kwambiri kumeneko, iye ndi mkazi wake, mpaka iwo anachita kumanga mahema kunja, kuti awasungiremo anawo."

²⁴ Ndipo ine ndinabwerera, ine ndinayamba kuganiza, "Inu mukudziwa, izo nzoona. Kuti, ndi—ndi munthu wamng'ono wodabwitsa." Ndipo ine ndikukhulupirira, M'bale Fleeman pano, ine ndikukhulupirira kuti mnyamata wake amapita ku Mpingo wa Faith Lutheran kumtunda kuno, mwamuna wamng'ono wodabwitsa ndi mkazi wake, iwo akuchita ntchito yopambana ya Ambuye. Ndipo ine ndinaganiza . . . Ine ndinayamba kutsuka galimoto yanga, ndipo ine—ine ndinakhumudwa. Ine ndinaganiza, "Nchifukwa chiyani kuti ine sindimatha kuchita zimenezo, mwaona, kumapita kumeneko, kukawatenga ana onsewo, nkumanditsatira ine kulikonse? Ine

ndimawakonda ana. Ndipo bwanji ine ndimalephera kumapita nyumba ndi nyumba, kuchokera msanamira kupita ku chipilala, monga choncho?”

²⁵ Ndipo Chinachake chinangondiuzwa ine, “Iwe sunaitanidwire zimenezo. Iye akungochita basi zomwe Mulungu anamuuza iye.”

²⁶ Koma ife tiyenera kukhala naye winawake ataima apa, monga Oral Roberts ndi iwo, Yoswa ali ndi lupanga, ali ndi Uthenga wa chikhulupiriro ndi chiwombolo. Ndipo, onani, ife tiyenera kukhala nawo iwo amene angakhoze kukhala nawo . . . mtundu umenewo, ndipo wina akhoza kukhala nacho *ichi*, koma zonse zimangopita palimodzi kupanga gulu limodzi lalikulu. Ndi Mpingo wa Mulungu.

²⁷ Ndikuyankhula mphindi pang’ono zapitazo kwa dona wamng’ono, wokhumudwa komanso wosweka mtima. Ndipo ine ndinali kuyesetsa kuti ndimuuze iye za momwe kuti—kuti mkazi ndi mwamuna sasiyanitsidwa, iwo ndi munthu mmodzi yemweyo. Munthu anapanga . . . Mulungu anapanga munthu, awiri onse mwamuna ndi mkazi; iye anali mwamuna. Uko nkulondola. Ndipo Iye anawalekanitsa iwo mu thupi ndipo anawapanga iwo mosiyana, koma anawalumikiza iwo pamodzi ndi kumalera ana awo, ngati mmodzi. Ndipo kotero mwamuna, wazimphamvu ndi waphula, ndipo mkazi ndiye—ndi—gawo la chikondi la mwamuna. Chotero, iwo amakhala limodzi. Ndizo . . . Mulungu anawalekanitsa iwo. Koma iwo onse anali munthu yemwe yemweyo, m-a-n. Ndipo mkazi amatchedwa woman, izo nzoon, chifukwa iye anatengedwa kuchokera kwa mwamuna. Iye ndi gawo la mwamuna. Koma mu—mu moyo kuno, mu thupi, iwo analekanitsidwa. Mu mzimu, iwo ndi mmodzi.

²⁸ Ndipo ndimayankhula za amuna kutaya chikondi chawo kwa akazi awo, ndipo samawakonda iwo monga ankachitira pamene iwo anali okonedwa. Manyazi pa inu. Inu muyenera kumachita zimenezo. Iye ndi wokonedwa wanu nthawizonse. Mwamtheradi. Ndiro gawo limene iye ayenera kukhala. Ndipo inu muyenera muzimukhazika iye monga choncho. Oh, musalole kuti chisangalalo chaching’ono icho chizitha, chifukwa icho sichidzatero, Kumwamba. Zidzangokhala mwangwirowi basi, Kumeneko. Uko nkulondola. Kotero onse . . .

²⁹ Chabwino, zikuwoneka ngati akazi ena ayenera kuti anati “ameni” kwa izo. Musadzati konse—musadzandilole konse ine ndidzamve, “Inu nthawizonse mumawalalatira akazi, ndi kumayankhula monga choncho.” Mlongo Hickerson, bwanji inu simunanene chinachake, kapena winawake kumbuyo uko, kunena . . .? Kodi munatero? [Mlongo Cox akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Zikomo inu, Mlongo Cox. Zimenezo ndi zabwino kwambiri. M’bale Cox, zimenezo ndi zanu, kulikonse kumene inu muli tsopano. Chabwino. Inde, bwana.

³⁰ Ndipo ife tisamaiwale kulemekezana wina ndi mzake. Nthawizonse tizikhala okondana. Musadzalole kuti izo zidzathe.

³¹ Mnyamata wa Chikatolika anabwera kwa ine, osati kale litali. Mkazi wake amalekana. Iye anati, “Billy, ine ndikudana nazo kuti ndibwere kwa iwe; ndine Mkatolika, ndipo iwe ndi wa Protestanti.” Anati, “Wansembe wandithamangitsa ine kuchoka kunyumba kwanga, kanthawi kapitako.”

Ndipo ine ndinati, “Chavuta ndi chiyani, Ham?”

³² Iye anati, “Chabwino, iye anandiuza ine.” Anati, “Ine ndimamwa pang’ono,” ndipo anati, “usiku, ine ndimagwira ntchito molimbika.” Anati, “Mkazi wanga akuganiza kuti ndiyenera ndizibwera usiku uliwonse ndi kudzamupsyopsyona iye, ndi kudzamukumbatira iye, ndi kumadzapanga ngati kuti tikukonzekera kuti tikwatirane.” Anati, “Ife tinakwatirana ndipo tiri ndi gulu la ana.” Ndipo anati, “Ife, ndiyo nthawi . . .”

³³ Ine ndinati, “Wuuu, dikirani miniti, mnyamata. Iwe ukulakwitsa. Iwe ukulakwitsa. Izo ndi zofanana basi ndi momwe zinaliri inu musanakwatirane. Mukuona? Iwe nthawizonse uyenera uzikumbukira zimenezo.” Ine ndinati, “Iye ndi wa usinkhu wa zaka forte tsopano, panthawi imene iye akufunikira chisamaliro chako.”

³⁴ Chotero, iwo anali ndi khoti la chisudzulo. Ndipo anati, “Ine sindikudziwa chimene ndingachite.”

³⁵ Ine ndinati, “Pita, ukamuyitane iye. Ngati ine ndingapite kunja uko, monga wa chi Protestanti, iye sakanandilandira ine. Koma ine . . . Mukuona?”

Anati, “Oh, iye amakukondani inu.”

³⁶ Ndipo ine ndinati, “Kuti, ingopita ukamuyitane iye, ukamuuze iye kuti wasintha malingaliro ako.”

³⁷ Ndipo chotero tsiku lotsatira, ine ndinali nditamuitana woweruza mulanduyo ndipo ndinayankhula naye iye. Ndipo ndinamuza mnyamata uyu, ine ndinati, “Ine ndidzakhala panso pomwe pamene woweruzayo azikakupatsa iwe mwayi woyankhulanso. Ine ndikakhala ndikukupempherera iwe. Usamuuze iye za izo.”

“Chabwino.”

³⁸ Chotero, ine ndinali kumusi uko, ndikupemphera. Patapita kanthawi ine ndinamva kulira kwakung’ono kwina kwake kukutsika masitepe, ndipo apa iwo anabwera, atakumbatirana mikono wina ndi mzake, akungomwetulira onse, inu mukudziwa. Iye anati . . . Ine ndinati, “Chabwino, moni, pamenepo!”

³⁹ Ndipo iye anati, “M’bale Branham, yakhala ili nthawi ndithu ndisanakuwoneni inu!” Eya, maminiti sarte, mwaona. “Kanthawi chikuwonereni inu!”

40 Ndipo iye anati, “Bwanji, M’busa Branham, ine sindinakuwoneni inu kwa nthawi yaitali! Ndakondwa kukuwonaninso inu!”

41 Ine ndinati, “Zikomo. Bwanji,” Ine ndinati, “inu mukuoneka ngati munali okondana.”

“Oh,” anati, “zikutiyendera bwino. Sichoncho ife, wokondedwa?”

Iye anati, “Inde, ife tiri, wokondedwa.” Ndipo ine...Iye anati, “Mudzabwere kudzatiwona ife nthawi ina, Abusa.”

42 Ndipo ine ndinati, “Zikomo inu, kwambiri.” Ine ndinati, “Tsalani bwino, inu!” Ndinawadutsa pamenepo, mnyamata wachikulireyo anatembenuka ndipo anabaibitsa mobwezera, monga *choncho*. Izo zonse zinachitika. Uko nkulondola.

43 Chikondi chimagonjetsa chirichonse. Uko nkulondola, basi—chikondi basi. Inu mukhoza kukhala nazo zizindikiro zanu zonse ndi maumboni, koma mungondipatsa ine chikondi. Izo—izo zimakhazikitsa izo, kwa ine. Oh, mai!

Wokondedwa Mwanawankhosa wakufa,
Mwazi Wanu wofunika
Sudzataya konse mphamvu Yake,
Mpaka Mpingo wonse woombodwa wa
Mulungu
Udzapulumsidwe, kuti usadzachimwenso.
(Mukuona?)

Chiyambireni mwa chikhulupiriro ine
ndinaona mtsinje umenewo
Mabala owukha Anu amapereka,
Chikondi chowombola chakhala mutu wanga,
Ndipo chidzakhhalapo mpaka ine nditafa.

Uko nkulondola. Oh, zodabwitsa!

44 Tsopano, zikumbutso zoyesedwa ndi nthawi! Kumene ine ndinapeza lingaliro ili mmawa uno, zinali kuchokera ku uthenga wathu wa Sande sukulu, uthenga wa uvangeli, kumene m’bale wathu amayankhula za Eliya. Kumene iye ankafuna... Anyamata awa, masukulu a aneneri, momwe iwo ankafunira kumanga mtundu wina wa sukulu yaikulu. Ndipo izo zinabwera ku malingaliro anga, ndipo ine ndinali kuganiza za malingaliro a “zikumbutso.”

45 Tsopano, chikumbutso ndi chi—chinthu chachikulu. Ife timayamikira zikumbutso. Ndipo amuna ambiri, mu moyo uno, ayeserapo kusiya kumbuyo kwawo mtundu wina wa chikumbutso. Pafupifupi amuna onse amakonda kuchita zimenezo. Amaika pamanda awo, chizindikiro chachikulu. Izo ndi zabwino. Zedi. Ine ndikuyamikira zimenezo. Ndizo—izo nzabwino. Ndiyeno ambiri amayesetsa kumanga makachisi akuluakulu.

⁴⁶ Chikumbutso chimodzi chimene ine ndikufuna kuti nditchulepo tsopano, chiri ku Ohio, ndipo uko kunali wachikunja. Ine ndaiwala dzina lake. Ine ndinapeza chithunzi chake kwinkwaka mu zotolera zanga kunyumba. Pamene, iye ankachitsutsa Chikhristu mwamphamvu, mpaka iye ankafuna kuti chikumbutso chimangidwe kwa iye, itachitika imfa yake, atapondetsa phazi lake pa Baibulo, akulozera pansu munga *choncho*, ndipo akuti, “Kutali ndi zikhulupiriro zachipembedzo, ndipo tiziikweza sayansi yamakono.” Ndipo pamene iye ankafa, iye anati, “Ngati ine ndalakwitsa, njoka zizidzakwawa zikutuluka kuchokera mmanda anga.” Ndipo pamene iye anafa, iwo anali ali mkati mponyera dothi m'manda ndipo anapha njoka zazikulu ziwiri kapena zitatatu. Ndipo lero, mmanda amenewo, mtumiki anajambula chithunzi posachedwapa ndipo anachibweretsa icho kuti adzandiwonetse ine, ndipo zikulendewera pa maunyolo pa manda ake... Mandawo ndi malo okongola, koma mtumbira wake sichina koma mtumbira wa njoka. Ndipo ziribe kanthu, ngakhale mu nthawi yophukira ndi yozizira, njoka zimakhala zikukwawabe kuchokera mmanda ake. Chikumbutso! Mulungu asadzandilore konse ine kudzakhalala ndi chikumbutso ngati chimenecho, kapena ali yense wa inu.

Chotero ziripo zikumbutso, ngakhale, zikumbutso zazikulu.

⁴⁷ Ine ndikuganiza za Yoswa, wankhondo wamphamvu. Iye anali munthu wamkulu bwanji, amene anatenga zida za Mose, munga mtsogoleri wa Ayuda mamillioni awiri awa. Mose pokhala wosankhidwayo, woitanidwa atuluke, wopatulidwira ku utumiki. Ndipo Yoswa, anadzalowamo ndipo anadzatenga malo a munthu ameneyo, ndithudi chinali chinthu chachikulu kuchichita, kuti akwaniritse nsapato za mneneri uyu. Wankhondo wamphamvu, woitanidwa, wokonzedweratu ndi wodzowedwa ndi Mulungu. Zaka foro handiredi iye asanabwere nkomwe, Mulungu anati Iye akanadzawapulumsa ndipo Iye akanadzawachezera iwo. Ndipo Mose anali wankhondo bwanji!

⁴⁸ Palibe munthu anayamba watengapo nsapato za Mose, kuti akwaniritse zimenezo, kufikira pamene Yesu Khristu anakhoza kuchita zimenezo. Ndipo iye anati, iyemwini, “Ambuye Mulungu wanu adzawukitsa Mneneri pakati panu, wonga ine. Ndipo zidzafika pochitika, ngati inu simudzamumvera Mneneri uyu, ali yense amene sadzamumvera Mneneri uyu adzadulidwa.” Chabwino.

Tsopano, chikumbutso chachikulu ichi.

⁴⁹ Ndipo Yoswa anali atatsikira ku mtsinjeko. Ndipo Mose atafa, Yoswa anadzatenga malo ake. Ndipo Mulungu anali ndi Yoswa. Ndipo iye anati, “Tsopano dzipatuleni nokha, muchape zovala zanu, ndipo mutalikirane, ndipo musayandikirane ndi

azikazi anu. Ndipo pa tsiku lachitatu, Mulungu akudzachita chinachake.” Oh, ine. . .

⁵⁰ Amodzi a mausiku awa, mautumiki a Lamlungu, ine ndikufuna ndidzalalikire za “tsiku lachitatu limenelo,” ndi kudzakuwonetsani inu mphamvu zomwe ziri mwa iwo, atatu amenewo. Ine ndazinena izo mmawa uno mu pemphero, aliynse amakhala ndi zinthu zitatu mu ziweregero za Baibulo.

⁵¹ “Tsopano, pa tsiku lachitatu inu mudzawona ulemelero wa Mulungu.” Tsopano izo kupita. . . zinapita kukawonetsa kuti iye ankadziwa bwino zomwe iye anali kuzikamba, chifukwa iye anatchula ndendende basi nthawi imene izo zikanati zidzachitikire. Ndipo ine ndikhoza kulingalira momwe Yoswa anamverera, pamene iye anaima pamenepo pamaso pa Aisraeli onse aja. Tsopano, mawu ake ayenera kukhala owona. Ndipo apo panali Yordani atafufuma.

⁵² Inu mwaona, khalidwe la munthu limadziwika ndi ntchito zake. Chirichonse chimene iwe uli, ntchito zako zimatsimikizira chimene iwe uli. Ziribe kanthu momwe ungachitire umboni, chirichonse chimene unganene, zabwino kapena zoipa, izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Ntchito zako zimanena chimene iwe uli, zimanena chimene iwe uli mkati. Ntchito iliyonse imene iwe ungachite, imawonetsera chimene iwe uli.

⁵³ Ndipo inu amuna amalonda, ngati inu mungogwira ntchito yamgwazo, onani chimene ine ndikutanthauza, ntchito ya theka chabe, musamachite zimenezo. Ngati inu simungathe kuichita iyo bwino bwino, musaichite iyo nkomwe. Uko nkulondola.

⁵⁴ Pamene inu mubwera kwa Khristu, ngati inu simungathe mwamtheradi kudzigulitsa, kudzitsekera, kuzidzazitsa, ndi kukhala mbiya, ndi kubwera kwa Khristu, musamabwere nkomwe. Koma pamene inu mukufunadi kukhala Mkristu, muziyima powonekera. Muzizipanga izo kukhala zenizeni. Ndi chimene Mulungu akufuna kuti inu muzikhala. Ndipo izo zidzatero—izo zidzatsimikizira, ntchito zanu zidzatsimikizira chimene khalidwe lanu liri. Khalidwe lanu limadziwika ndi ntchito zimene inu mukuchita.

⁵⁵ Ndipo Yoswa, tsopano, mawu ake anali pa chiwopsyezo; inde, bwana, chimodzimodzi monga—monga Nowa wakale. Koma Yoswa ayenera awoloke mtsinje uwu. Ndipo zikuwoneka ngati anasankha nthawi yoyipitsitsa yomwe ingaganiziridwe konse. Unali mwezi wa Epulo. Ndipo ndi pamene chisanu chimasungunuka mu Yudeya, ndi kumabwera kumatsikira mmapiri, ndipo Yordani wakaleyo ndi wa matope, ndipo amafalikira mpaka kukalowa—mminda, kukathirira minda ya Yordani. Ndipo zimawoneka ngati, ngati izo zikanakhala mwamasamu, kapena—kapena mwamaphunziro, kapena mwasayansi, iye—iye anasankha nthawi yoipa kwambiri mchaka chonsecho yowolokera Yordani. Koma Mulungu amakonda

kutenga nthawi za mtundu umenewo kuti atsimikizire kuti Iye ndi Mulungu.

⁵⁶ Ndipo anthu a Mulungu, amene amakhulupirira Mulungu ndi kudziwa zimene Mulungu walonjeza, samawopa kuchita izo, chifukwa Mulungu adzamatirana ndi Mawu Ake, motsimikiza basi monga Iye ali Mulungu.

⁵⁷ Ndipo pamene iye anati, “Choyamba, tengani likasa ndipo muzipita patsogolo.” Ndipo pamene mapazi a ansembe amenewo anakhudza Yordani uja, zinalibe kanthu momwe iye analusira, ndi momwe iye amafufumira, iye anapereka njira ku Mawu Amuyaya a Mulungu, pakuti Mawu anali mu likasa. Yesu anati, tsopano, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita konse.” Chotero, Yoswa, podziwa kuti mawu ake ayenera kutsamira pa Mawu a Mulungu, ndipo iye anayika Mawu a Mulungu akhale poyambirira.

⁵⁸ Ine ndikukhumba anthu odwala inu pano usikuuno mukachita zimenezo, muwaike Mawu a Mulungu ndi chivomerezo chanu. Muike chivomerezo chanu, inu mukhulupirire zimenezo ndipo mukaziike izo pamenepo; ndi kudziticha zinthu zimenezo, zimene palibepo, ngati kuti ziripo. Ndiye kuti ife tikuguba chitsogolo. Muchite izo mwanjira imeneyo. Mawu a Mulungu adzazidutsitsa izo.

⁵⁹ Ndipo pamene mapazi a ansembe anakhudza Yordani, iye anangodzafunulira mmbuyo, mbali ndi mbali. Ndipo madzi anakhazikika.

⁶⁰ Kodi inu mukuzindikira? Kubangula kwa mtsinje umenewo kukanabweretsa gombe pamenepo, mu nthawi ya maminiti twente, likanakhala lalikulu monga—monga ena a madziwe aakulu amakono awa omwe ife tiri nawo, ndi Damu la Colorado Boulder kunjira uko. Momwe Yordani amasesera kudutsa kumeneko, akamabwera kuchokera mmapiri, ndi mphamvu yaikulu, ndipo iye akusesa kudutsa mu zigwa zimenezo.

⁶¹ Ndipo pamene anthu oyenda pansu thuu milioni, ndi akazi ndi ana, ochuluka kumeneko, mwinamwake anatenga maora foro kapena faivi, kapena kupitirirapo. Ndipo kodi inu mukuganiza chiyani? Mtsinje umenewo ukanadzaza. Koma, Mulungu anawuimitsa mtsinjewo. Amen. Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. Anaimitsa mitsinjeyo! Ndipo iwo unakhala pamenepo mpaka iwo atawoloka.

⁶² Zitatero Mulungu anati kwa Yoswa, “Ife tikufuna tipange chikumbutso kwa izi. Pita kunjira uko ndipo ukantumize m’Israyeli aliyense, mmodzi kuchokera mu fuko, ndipo akatenge miyala thwelofu ndipo ukapange chikumbutso. Ndipo chikumbutso ichi chidzakhala kuti pamene ana anu akudutsa njira iyi, iwo azidzafunsa, ‘Nchiyani chinapangitsa miyala iyi kuti ipezeke apa?’ Ndipo iwe uzidzawauza iwo nkhani ya mmene

Mulungu anaimitsira mtsinje wa Yordani.” Chimenecho ndi chikumbukiro chodabwitsa. Tsiku lina ine ndikuyembekeza kudzayang’ana pa miyala imeneyo, posachedwapa, kumene iyo ikuimabe ngati chikumbutso. Komano ine ndimaganiza za—za chikumbutso china. . . Chimenecho chinali chikumbutso chachikulu chodala bwanji!

⁶³ Ndiye ine ndikuganiza za chikumbutso china, tsiku lina, pamene mkazi anapanga kusankha kolakwika. Iye anaganiza kuti asakhale mu zigwa zokhala ndi madzi ambiri za—za, kapena, kuti azikhala mu zigwa zothiridwa madzi za Sodomu ndi Gomora, ndi kukakhala wochezeka ndi kumakhala monga momwe akazi ena ankakhalira mmasiku amenewo.

⁶⁴ Iye sanatenge kusankha kwabwino, monga Sarah amene anakakhala mmaiko owuma. Kokha, iye anawasunga Mawu a Mulungu mu mtima mwake. Ndipo iye anali womvera ndi wokondedwa kwa mwamuna wake, mpaka kuti iye ankamutcha iye “mbuye” wake. Ndipo apo ndi pamene Mulungu anadzatsika ndi Angelo awiri ndi kudzawachezera iwo mu hema.

⁶⁵ Koma, Mkazi wa Loti, iye anadzakhala wachidziko kwambiri ndipo anatengeka ndi zinthu za mdziko. Ndipo ndi phunziro bwanji kwa ife, lero, kuti ife tikhoza kukhala amalingaliro achidziko. Ndipo ine ndiri wotsimikiza ndithudi, lero, kuti mpingo, mwathunthu, ukukhala wamalingaliro achidziko kwambiri. Tsopano, mwinamwake, Mkazi wa Loti sankatanthauza kuti achite zimenezo, pamene iye anapita kumeneko. Iye anaganiza, “Ndingokhala wochezeka basi.” Ndi zabwino kukhala wochezeka, koma musatengere zizolowezi za mdziko.

⁶⁶ Pamene inu mukupita, muzipita monga Shadreki, Misheki, ndi Abedinego, ndi Daniele. Iwo anatsimikiza mu mtima mwawo kuti iwo sadzadzidetsa okha, ziribe kanthu zimene zingabwere kapena kupita. Ziribe kanthu kaya mpingo wonsewo unabwerera mmbuyo, chimene chinachitika, iwo anatsimikiza mu mtima mwawo. Ndipo iwo ndi chikumbutso lero.

⁶⁷ Ndipo Mkazi wa Loti amaimira chikumbutso. Ndipo pamene Mulungu anamupatsa iye uthenga wake wotsiriza wa chisomo, pamene Iye anawatumiza Angelo awo kumeneko ndipo nkuwauza iwo kuti mkati mwa maora pang’ono kuti Sodomu ndi Gomora adzawotchedwa, komabe, iye sanathe kupirira nalo lingaliro losiya moyo wake wamanyado, kuti atuluke apite mchipululu, ndi kukakhala monga Sarah ankakhalira kunja uko mu chipululu, ndi kumakavala zovala wamba, zovala wamba za mkazi wakuchigwa. Iye ankafuna kukhala mzisangalalo. Mwamuna wake anali atakhala munthu wotchuka mu mzindawo. Iye amakhala pa chipata, monga woweruza kapena ngati meya wa mzinda. Ndipo iye ankafuna zisangalalo izi. Ndipo iye sakanakhoza kukwanitsa kutenga lingaliro

lakuti azisiye zinthu zimenezo. Ndipo pamene iye ankapita ndi mwamuna wake, akutuluka mu mzindawo, iye anapitirira kumayang'ana m'mbuyo, akulira ndi kumakhumudwa chifukwa iye amazisiya zimenezo, kuti adzilekanitse yekha ku mtundu umenewo wa imfa.

⁶⁸ Yesu anati, “Iye amene aika dzanja lake pa khasu, ndipo ngati atembenuka kuti awone mmbuyo, sali woyenera kulima.” Ndi mtundu wanji wa anthu womwe ife tikuyenera kukhala? Iye amene ayika dzanja lake pa khasu, ndipo nkomwe osati—osapotoloka mmbuyo, koma akangopotoloka kuti ayang'ane mmbuyo, si woyenera nkomwe kuti azilima. Oh, tiyenera kumaika maso ndi mitima pamodzi. Ziribe kanthu zimene anthu enawo akuchita, zomwe mpingo ukuchita, zomwe woyandikana naye akuchita, zomwe wina aliyense akuchita, muziika mtima wanu pa Gologota. Musamaimo nkomwe ndi kuyang'ana mmbuyo. Ife tiribe nthawi yomayang'ana mmbuyo.

⁶⁹ Ndipo mkazi uyu, chifukwa iye anatero, Mulungu anapereka chikumbutso kwa anthu onse amene amatembenuka ndi kuyang'ana mmbuyo, iwo atatha kumulandira kale Khristu ngati Mpulumutsi wawo. Iye anasanduka chulu cha mchere. Ndipo iye ali pamenepo mpaka lero, izo zikhoza kuwonedwa m'minda, mkazi atayima pamenepo atapotoloka mutu wake, akuyang'ana mmbuyo. Ndipo iye akuyang'ana mmbuyo pa phewa lake lakumanzere, kuti ayang'ane mmbuyo m'minda. Mtima wake unali kumbuyo uko. Komabe, iye anakakamizika, monga momwe zinakhaira, kuti achite izi.

⁷⁰ Ndipo anthu ambiri amamutenga Khristu mwanjira imeneyo, lero, chifukwa iwo amatuluka kuchokera mdziko, akumverera ngati kuti achita kukakamizidwa kuti achite zimenezo. Ndipo iwo amakhala akulakalala ndi kusilira, ndipo sipamatenga nthawi kuti iwo abwerere mmbuyo. Ndipo iwo—iwo ndi zikumbutso zowopsya za chisomo cha Mulungu, za chikondi cha Mulungu monga chinawonetseredwa kwa iwo. Tsopano, zikumbutso!

⁷¹ Tsopano, m'masiku a Yesu, ali padziko lapansi, Ayuda anali atamanga kachisi ngati chikumbutso. Ndipo anali atamuwonetsa Yesu mmene kachisiyo anamangidwira bwino. Ndipo Iye anati . . . Zinatenga zaka forte kuti amange kachisiyo; pafupifupi zaka eyite, pamodzi. Kwa zaka forte, iwo anali akudula miyala m'madera osiyanasiyana a dziko lapansi. Zaka forte mukumangidwa kwake, popanda phokoso la macheka kapena phokoso la nyundo.

⁷² Koma, inu mukudziwa, ngakhale Yesu ananena pamenepo, “Musayang'ane pa ichi, pakuti ine ndinena kwa inu, kuti padzafika nthawi imene sipadzakhala mwala umodzi udzasiyidwe pa umzake, mwala umodzi pa umzake.”

⁷³ Basi asanati, Iye asananene Mawu aakulu achikumbutso awa, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, akachisi adzapita, zikumbutso zidzapita, koma Mawu Anga ndiwo chikumbutso chosatha.”

⁷⁴ Chombo chinavunda, zaka zapitazo. Manda a aneneri anagwera mkati. Ndipo zikumbutso zonse zosiyanasiyana zinavunda, ndipo nthawi yotopetsa, yasesa mwalawo. Koma Mawu a Mulungu akukhalabe chimodzimodzi, okongola kwanthawi za nthawi. Amoyo ndi atsopano usikuuno, kwa okhulupirira a tsiku lino, monga Iwo ankakhalira mmasiku amene Iwo anayankhulidwa.

⁷⁵ Nzosadabwitsa, Eliya, mmawa uno, mu wathu. . . uthenga umene m’bale wathu anatipatsa ife. Pamene iwo ankafuna kuti amange sukulu yaikulu ya aneneri, ngati chikumbutso, koma Eliya anasankha chinthu chabwinoko, chozizwitsa cha Mulungu kudzutsa chida chakugwa ndi kuchipanga icho kusambira pa madzi. Iwo anali Mawu a Ambuye.

⁷⁶ Ndipo wabwinoko ali iye, usikuuno, yemwe alandire Mawu a Ambuye, mu mtima mwake, kukhala chikumbutso, kuposa iwo omwe angamayesere kuti akhazikitse chikumbutso china chachikulu.

⁷⁷ Osati kale kwambiri, pamene ine ndinamva, pamene ine ndinali ku Italy, ine ndinamva za Mussolini, ndi choimikidwa chachikulu chija cha mapazi forte chakuti mmwamba, chimene iye anachimanga ngati chikumbutso kwa othamanga, pakuti iye anali wothamanga. Ndipo ine ndinkafuna kuchipeza chikumbutso chimenecho. Ndipo, inu mukudziwa, icho chinali chitaphulitsidwa kukhala ufa ndi chophulitsa miyala chachikulu.

⁷⁸ Ine ndinaima, pafupifupi zaka ziwiri, zitatu zapitazo, pa malo pamene afarao aku Igupto anadzutsa makachisi aakulu ndi mafano. Ndipo ine. . . Iwo amandiuza ine kuti uyenera kukumba mapazi twente pansi pa nthaka, kuti ukapeze ngakhale pansi pomwe zikumbutsozo zinaima.

⁷⁹ Ine ndinaima pamene Kaisara Augusta, kumene Herode ndi wamkulu wa Roma. Ndipo ine ndinapita mu msewu, ndipo kumene iye anakonda kupitako kumusi kwa msewu kuchokera ku nyumba yachifumu, ndipo ndi pafupifupi mapazi twente-faivi pansi pa nthaka. Zikumbutso zimenezo zinapita.

⁸⁰ Koma Mawu amoyo amenewo a Mulungu akadali chimodzimodzi basi ndi ofunika basi. Ndicho chikumbutso.

⁸¹ Chotero ine ndikunena, lero, m’bale, zomwe inu mumachita, mawu omwe mumanena, momwe inu mumachitira nawo amzanu, ndipo zimene inu mumachita zokhudza Khristu, zidzakhala chikumbutso chosatha. Iwe ukhoza kukhala ndi nyumba yabwino yowasiyira ana ako. Inu mukhoza kumagwira ntchito kuti muzipeza chakudya, kuti muwasiyire ana anu.

Koma ine kulibwino ndiwasiyire iwo Mawu a Mulungu kuposa china chirichonse. Nyumba zimenezo zidzatha. Ndizo zangwiro zabwino, ndizo zabwino. Ine ndiribe kanthu kotsutsa izo. Koma musamachite zinthu zazing'ono zimenezo ndi kusiya zinthu zazikuluzo zosachitidwa, inu mwaona. Chifukwa, Mawu adzatero...Nyumbayo idzawonongeka, ndipo anthu adzawonongeka limodzi ndi iyo. Koma Mawu a Mulungu adzawaukitsa iwo mmasiku otsiriza, ndi kudzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya ndi wachisavundi kachiwiri. Ndipo, tsopano, polinga kuti apange cholowa monga chonchi, Mawu Amuyaya a Mulungu!

⁸² Ine ndikuganiza za nyimbo yakale iyi imene tinkakonda kuiyimba kuno, zaka zapitazo:

Nthawi yadzaza nazo zosinthika mwaliwiro,
 Palibe chosasuntha chingaima,
 Mangani ziyembekezo zanu pa zinthu
 Zamuyaya,
 Gwirani pa dzanja la Mulungu losasintha!
 Pamene ulendo wathu udzatha,
 Ngati kwa Mulungu takhala owona,
 Kunyumba kwathu ku Ulemelero ndi kowala,
 Solo yathu yokwatulidwa idzawona!

⁸³ Nkwabwino bwanji kuyang'ana kunja, pamene kulowa kwa dzuwa kukuwonekera, pamene mitsempha yanu ikuzizira mthupi mwanu, pamene ana anu atayima mozungulira bedi, kumadziwa kuti iwe unamanga chikumbutso, chimenecho, “Wokonedwa, tsiku lina adadi adzakumana nawe kutsidya linalo!” Ine ndingakonde nditakhala ndi zimenezo.

⁸⁴ Pamene dokotala atati, “Billy, palibenso china chomwe chingachitike kwa iwe.”

⁸⁵ Ndipo ine nkumawawona ana anga, ndipo nkuwapsyopsyona iwo tsalani bwino. Ine nkuti, “Koma adadi sakufa. Iwo akupita kokapumula, ku Malo. ‘Pakuti ngati msasa wapansi pano upasuka, ine ndiri nawo wina ukudikirira.’” Ndi chikumbutso bwanji kuti uchiyankhule momveka! Ine kulibwino ndichite zimenezo, pamaso pa ana anga, kuposa kunena kuti, “Wokonedwa, ine ndiri ndi madola milioni ku banki *iyi*, ndi milioni cha kuno mu *iyi*, ya iwe.” Ine ndingakonde nditasiya umboni umenewo.

Ndi zikumbutso, zimene tizisiya mmbuyo
 Mphondero mu mchenga wa nthawi;
 Mphondero, kuti mwinamwake wina,
 Akuyandama panjira ya moyo wokwiya,
 Ya m'bale wosimidwa ndi wa ngalawa
 yophwasuka,
 Pakuwona, adzagwire mtima kachiwiri.

Mwamtheradi! Kuzisiya izo zikhale chikumbutso, maumboni anu.

⁸⁶ Momwe ine ndikuganizira, usikuuno, za bambo wachikulire yemwe wagana kutsidyako, mu maora ake utsiriza a moyo uno, anandiyitana tsiku lina ndipo akufuna kuti ine ndidzalalikire maliro ake; Kachisi wa Paul Rader's. Ameneyo ndi mzanga wabwino, F. F. Bosworth, woyera waumulungu akupita kukakomana ndi Mlengi wake. Ndipo iye anati, "Iyi ndi nthawi yosangalatsa kwambiri ya moyo wanga, M'bale Branham." Iye anati, "Ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti ine ndidzakumana naye Iye, ine sindikutha kugona usiku."

⁸⁷ Ine ndinamvapo za Akazi a Aimee McPherson; sikuti ndikumunyazitsa iye, mkazi wodabwitsa. Ine ndikuwona zimene anasiya *uyu* ndi *uyo*. Ine ndikuwona zimene anasiya Smith Wigglesworth ndi Dr. Price, ndi ambiri a amuna otchuka amenewo, koma palibe chosiyidwa chimodzi chimene ine ndinamvapo aliyense akunena cha F. F. Bosworth. Mulungu, mulole mathero anga adzakhale monga choncho, chikumbutso cha chisomo cha Ambuye Yesu Khristu!

⁸⁸ Ine ndikuganiza za E. Howard Cadle kumtunda kuno, osati kale litali, pamene iye anali atagona pansi, ngati woledzera, ndipo a—ndipo ntchentche zikuwulukira mkamwa mwake. Ndipo amayi ake okonedwa achikulire kumusi uko anali atapemphera ndi kukhulupirira, ndipo anagwiritsitsa kwa Mulungu, chifukwa cha mnyamata wake woledzera. Kumeneko, pamene iye analisisa dziko, iye anasiya umboni ndi chikumbutso cha chisomo cha Mulungu Wamphamvuzonse chimene chiri chokwanira. Pamene Mawu a Mulungu ayikidwa kwa Iye, mu pemphero, Mulungu ayenera kuyankha pa zimenezo.

⁸⁹ Mulungu akumanga Mpingo kukhala chikumbutso, chikumbutso cha nsembe Yake. Khristu sanabwere padziko lapansi kuti adzafe pachabe. Imfa yake siidzakhala pachabe. "Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu." Ngati anthu sakhala moyo Iwo, ngati iwo sangawatenge Iwo ndipo, pansi pa kulingalira, ndi kuzindikira mphatso yaikulu bwanji imene Mulungu wawapatsa iwo, Mulungu ndi wokhoza mwa miyala kudzutsira ana kwa Abrahamu. Ndithudi Iye adzachita zimenezo! Ndipo pamene ine ndiganiza za zimenezo, ndi kuganizira za mtengo waukulu umene Iye ankayenera kulipira! Tsopano zabwino . . .

⁹⁰ Aliyense amafuna chirichonse chaulere, amafuna chirichonse. . .Ndiko kachitidwe kamoyo ka America lero. Kupeza zonse zomwe ungate mwaulere. M'bale, sumapeza kalikonse ka mtengo uliwonse, pachabe. Iwe umalipira zomwe wazipeza. Uko nkulondola. Iwe umayenera kuzilipira izo, ndipo izo zimabwera ndi mtengo.

⁹¹ Ndipo chipulumutso chanu chinabwera ndi mtengo, kwa Mulungu. Izo zinamtengera Mwana Wake wobadwa yekha, kuti adzapereke Moyo Wamuyaya kwa munthu aliyense ndi kumupangitsa iye azikondwa, usikuuno, ndi kukhalira moyo zinthu zoyenera kuzikhalira moyo. Osati kuwasiyira ana athu chinachake; palibe cholowa chimene chingasiyidwe, kuposa chipulumutso cha Ambuye wathu Yesu. Ndithudi, sichoncho izo.

⁹² Tsopano, mtengo wawukulu walipidwa. Kuyesedwa kwa nthawi kuyenera kubwerapo. Ndi zikumbutso zoyesedwa ndi nthawi. Ndipo chikumbutso chokhacho chimene chinayamba chayesedwapo molondola, chakhala chiri Mawu a Mulungu. Oh, achikunja ayesetsa kuchizimitsa Icho. Iwo achita chirichonse chimene iwo akanakhoza kuchita, koma Icho sichidzatha konse. Icho sichingakhoze konse kulephera.

⁹³ Abrahamu, pamene iye analandira chikumbutso cha Mulungu icho, “Iwe udzakhala ndi mwana mwa mkazi ameneyo, Sarah.” Zaka twente-faivi, iye anakhulupirira zimenezo ndi mtima wake wonse, ndipo anakana chirichonse chosiyana ndi icho, pakuti iye ankadziwa kuti Mulungu akanadzazungu Mawu Ake.

⁹⁴ Achikunja, lero, iwo amawuka ndi kuyesera kulipaka Baibulo. Inu musanati muimitse Baibulo, inu mukanayenera kuiyimitsa nthawi inu musanachite zimenezo. Dziko lirilonse losakhulupirira, anthu aliwonse osakhulupirira, anthu achikominisi onse, ndi chirichonse chimene iwo ali, wa Buddha aliyense, wa Jain aliyense, wa Chimuhamadi aliyense, ayenera kuchitira umboni kubadwa kwa Ambuye Yesu Khristu, tsiku lirilonse. Chabwino, nthawi iliyonse imene musaina kalata, ameni, nthawi iliyonse mulemba deti, inu mumachitira umboni kuti Mulungu anatuziza Mwana Wake, zaka naintini handiredi ndi fifite seveni zapitazo. M’bale, inu simukanakhoza kuchita zimenezo. Izo sizikanakhoza konse kukhala. “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita konse.”

⁹⁵ Nthawi ina kalelo, ine ndinali ku New York, ndinapita pa chilumba chaching’ono, ku Statue of Liberty chimene chinaperekedwa kwa a...ndi boma la France, ku United States, zaka zambiri zapitazo. Ndipo mdzanja lake muli nyali yoyaka. Ife tinapita ku nkono umenewo. Pamenepo pali zenera pamenepo. Ndipo pamene kuwala kwakukulu uku kunali kuwalira, ine ndinazindikira kumusi kumbaliko kunali gulu la mpheta zazing’ono, ndipo izo zonse zinali zitafa, zitagona chakumbali. Ndipo ine ndinati kwa namulondola, “Kodi mphetazo ndi chiyani? Kodi izo zaphedwa ndi magetsi?”

⁹⁶ Anati, “Ayi, bwana. Ife sitinazitole izo panobe mmawa uno.” Anati, “Usiku watha kunali mkuntho, mkuntho waukulu unabwera kudutsa pagombe kuno.”

Ine ndinati, “Inde, bwana. Ine ndikudziwa zimenezo.”

⁹⁷ Iye anati, “Tinthu tating’onoto tinagwidwa mu namondweyo.” Ndipo anati, “Pamene tinadzafika mu kuwala uku, ito timayesera kuti timenye nkuzimitsa kuwalako. Mukuona? Ito timangogunda pa galasi ili ndi kumamenya.” Ndipo anati, “M’ malo mogwiritsa ntchito kuwalako kuti tipite kumalo otetezeka, ito timayesetsa kuzimitsa kuwalako.”

⁹⁸ Ndiyeno kudzoza kunadzandikhudza ine. Uko nkulondola. Amuna ndi akazi amene akuyesetsa kuti azimitse Kuwala kwa Mulungu, akungozimitsa ubongo wawo womwe. Ndipo, Kuwala, bwanji iwo sakugwiritsa ntchito Iko kuti apitire nako ku chitetezero, mmalo momenya ubongo wanu? Kuyesetsa ndi kuwakana Iwo, ndi kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu chotero monga machiritso Auzimu, kulibeko chipulumutso chokhudza mtima, zinthu zimenezi.” Iwo akungomenyetsa pa chikhomo. Bola ngati iwo akuchita zimenezo, Mpingo waukulu wa Mulungu ukusunthira chitsogolo ndi mmwamba, mwamphamvu basi monga iwo ungakhoze kuchitira. Anthu amawuka ndi kumadzinenera kuti ali *ichi*, ndi *icho*, ndi kumalephera, ndi zina zotero. Koma Mpingo wa Mulungu umasunthabe chitsogolo, ndipo Mawu a Mulungu umasunthabe chitsogolo. Iwo unapangidwa kuchokera ku chipangizo choyenera.

⁹⁹ Osati kale litali, uko mu Australia, Australia wopambana yemwe ali pansi pa korona wa Britain, ali ngati South Africa, kungodutsa njira yopita ku Australia. Uko mu Sydney, kuli mzinda waukulu umene umabwera mozungulira gombe kumeneko, M’ bale Beeler mwinamwake akudziwa zambiri za izo kuposa ine. Komabe, iwo ankafuna kumanga mlatho, wotalika kuyambira—kuyambira ku North Sydney kupita ku South Sydney. Iwo anaitana dziko lonse, kuti apeze amisiri, omanga milatho, kuti abwere adzamange mlatho uwu. Palibe m’modzi wa iwo amaitenga iyo. Palibe mmodzi anayerekeza kuti achite zimenezo. Mwamsanga pamene iwo atafika kumeneko, iwo anakapeza kuti pansi pa nyanjayo panali mchenga wosakhazikika. Iwo unali mchenga wosunthasuntha, ndipo palibe chimene chimaima. Ndipo iwo anaziyeza izo ndipo anawomba, ndipo anapitirira. Iwo anati, “Ayi, ife sitingathe ngakhale kuyesera kuti timange mlatho woterowo. Izo sizingakhoze kuchitidwa.”

¹⁰⁰ Patapita kanthawi, mmisiri wachichepere wochokera ku England anadzafika, munthu wotchuka, munthu wambiri yabwino, anali ndi mbiri yabwino.

¹⁰¹ Oh, ine ndikuzikonda zimenezo! Ine ndimakonda mwamuna yemwe ali ndi mbiri yabwino. Oh, iwe sumayenera kukhala munthu wamkulu. Iwe ukhoza kukhala wopemphetsa yemwe amakhala mngalande, ndipo nkukhala ndi mbiri yabwino kuposa wamphamvu. Mwamtheradi. Iwe sumasowa kuti ukhale wolemera. Iwe ukhoza kungokhala ndi mbiri yabwino.

Izo zimalengeza, mbiri yako yabwino ndi chimene iwe uli, zimakupanga iwe chimene iwe uli. Izo zimakupatsa iwe mbiri yako yabwino. Ndipo iwe umadziwika ndi mbiri yako yabwino.

¹⁰² Munthu uyu anapita kumeneko ali ndi mbiri yodabwitsa. Iye anayang'anitsitsa mmene ziliri. Iye anayenda mmagombewo kwa masiku angapo. Iye anaphunzira izo. Iye anapima. Iye anawomba. Iye anayang'ana pozungulira. Patapita kanthawi, iye anapita kwa ameya, anati, "Ine ndiyigwira ntchitoyi."

"Bwanji," iye anati, "bwana, inu mukudziwa zomwe mukutengazi?"

Iye anati, "Ine ndikumvetsa bwino bwino."

¹⁰³ Iye anati, "Chabwino, mmisiri wamkulu uyu anati... Amisiri aku America ndi amisiri ochokera konsekonse padziko lapansi, omanga milatho, abwera kuno, ndipo iwo ayiwopa ntchitoyi."

¹⁰⁴ Iye anati, "Koma, bwana, ine sindikuiwopa ntchitoyi. Ine ndiyitenga iyo." Iye anati, "Ine ndikudziwa kuti ndiri ndi mbiri ya padziko lonse, ngati womanga mlatho; koma ine ndiyika mbiri yanga pachiswe, pakuti ine ndikhoza kuimanga iyo." Oh, iye anali ndi masomphenya! Munthu asanapange mbiri, iye amayenera kukhala ndi masomphenya a zomwe iye akupangazo.

¹⁰⁵ Oh, adalitsike Ambuye! Ndi chifukwa chake kuli Kumwamba kuti tidzapiteko. Ndi chifukwa chake ife tikhoza kukhala ndi mbiri monga Mkristu, ife timadziwa chipangizo chimene chiri mnyumbayi. Uko nkulondola. Ndi Magazi a Yesu Khristu ali mnyumba ino. Uko nkulondola. Magazi Ake amadontho atsuka machimo onse. Iye anandichotsa ine mngalande za ku gehena ndipo anandipanga ine kukhala wanchito Wake. Ndiye, ine ndimakhulupirira mwa Iye. Chotero, ine ndadutsa kuchoka ku imfa ndapita ku Moyo. Ndipo wokhulupirira aliyense wachita zimenezo, chifukwa chakuti iwo ali ndi chidaliro ndipo iwo amakhulupirira mwa Womanga wamkulu uyu, ndi Mmisiri wamkulu uyu.

¹⁰⁶ Tsopano, pamene mwamunayo anachita zimenezo, chinthu choyamba chimene iye anachita, kuti akhale wotsimikiza kuti iye anali wolondola, iye anapita kumeneko. Ndipo iye anati, "Tsopano, ife tisanayambe mlatho uwu, ife tiyenera kupita ku maziko olimba. Ife tiyenera tipite." Iye ankadziwa kuti pansu pa mchenga umenewo, pachifuwa cha nthakayo panali pamenezo, chimene chinali mwala wolimba. Iye anachita chiyani koma kupeza mapampu akuluakulu? Ndipo analowa mmenemo ndipo anakakhazika machubu akuluakulu pansu, ndipo iye anapopa mchenga wosunthasunthawo, ndi mapampu amenewa, kufikira kuti iye anawusuntha iwo mpaka kufika pa thanthwe lolimbalo. Pamene iye anazifikitsa izo pa thanthwelo, iye anazika mabawuti akuluakulu awa pamenezo, ndipo anazikonzekeretsa izo. Ndipo iye anasuntha uliwonse.

107 Ndipo kenako iye anapita ndipo anakatenga, omuzungulira iye, amisiri opambana kwambiri omwe iye akanakhoza kuwapeza, asayansi abwino kwambiri, zida zabwino kwambiri. Iye anatumiza ndipo anakatenga zitsulo za mlatho wake. Pamene iye anachita izo, iye sakanaika chidutswa chimodzi cha chitsulo, osati ngakhale bawuti imodzi, mpaka icho chitapimidwa mwasayansi; kuti awone ngati munali kupuma kulikonse mmenemo, kuti awone ngati munali timabowo tating'ono ta mpweya mmenemo, mu chipalacho, mmene iwo amapangira izo ndi kuziwumba izo, kuti awone ngati izo zinapimidwa moyenera. Oh, chiyani a—ndi chikumbutso chotani icho chikanakhala, ngati...ku mbiri yake monga womanga mlatho.

108 Ngati iye anapita ku vuto lochuluka limenelo, kuti akhale wotsimikiza kuti mlathowo ukhala wotetezeka, ndiye inu mukuganiza kuti ndi vuto lochuluka bwanji limene Mulungu anapitako, kuti akatsimikizire kuti Mpingo uwu ukhala wotetezeka? Inde, bwana. Chiripo chikumbutso ku imfa ya Khristu, umenewo ndi Mpingo Wake. Anthu ena samafuna kuwukhala moyo, anthu ena amawukhala. Koma, ndi nthawi yoyesera. Mulungu akuwayesa anthu, lero, kwa zikumbutso Zake.

Nthawi zambiri, anthu amati, “Oh, ine ndayesedwa kwambiri!”

109 Lidalitsike Dzina la Ambuye, chifukwa cha mayesero! “Pamene ine ndiri wofooka, ndiye kuti ndiri wamphamvu,” anatero Paulo. “Mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu, amayenera poyamba ayesedwe ndi kuyesedwa.” Ndipo kuyesedwa kumeneku ndi kokoma kwa inu, ndi kokonedwa kwa inu, kuposa golide wamtengo wapatali. Ndi nthawi yoyesedwa.

110 Zaka zambiri zapitazo, asanakhale ndi zosungunulira, iwo anakonda kumutenga golide...Ndipo momwe iwo anakdziwira kuti ndi weniweni kapena ayi, ndipo litsiro lonse amalichotsapo, chitsulo chonse cha galasi (uyo ndi golide wabodza), zopusitsa zonse amazitultusamo, iwo...Omenya amammenya iye, ndipo amammenya iye ndi kumutembenuza iye, ndi kumumenya iye ndi kumutembenuza iye, mpaka womenyayo amawona chake—chinyezimiritso chake mu golideyo.

111 Umo ndi momwe Mulungu amachitira ndi Mpingo Wake. Iye amakupatsani inu mayesero pambuyo pa mayeso, mayeso pambuyo pa mayeso, mayeso pambuyo pa mayeso, mpaka Moyo wa Khristu utawonekera mu moyo wanu; mpaka inu mutakhala wamtendere, wodziletsa, wofatsa, wodekha, wodzichepetsa, wokonzeka, womvera, wololera, wotembenuza mutu wanu kuwuchotsa ku zinthu za mdziko, ndi kuyang'ana molunjika ku Kalvare, kwa Mmodzi

Yemwe akuchita kumenyako. Nthawi zambiri inu mumaganiza kuti ndi zachilendo chifukwa cha mayesero amoto, matenda, ndi mazunzo. Izo zimangochitika kuti akuyeseni inu, kuti achotse litsiro pa inu, kuti atulutsepo matope mwa inu, kuti achotsepo chidodo mwa inu, kuti akudzutseni inu kufika kumalo amene mungayang'ane ndi kuwona chinyezimiritsocho, kapena munthu kukhoza kuwona chinyezimiritso cha Khristu mwa inu, “Khristu mwa inu, chiyembekezo cha Ulemelero.”

¹¹² Iye anayesa chidutswa chirichonse. Pomaliza, iye...Iye asanaike bawuti, iye anayesa izo. Iye anayesa chirichonse.

¹¹³ Ndiye pamene iye anamalizitsa izo zonse, tsopano, onyozawo anaima pafupi ndipo anati, “Izo sizikhalitsa. Izo sizingakhoze kuchita izo.”

¹¹⁴ Ndizo zimene iwo akunena lero. “Ichi apa chipembedzo cha Mzimu Woyera chimene inu mukuchikamba, izo sizitenga nthawi yaitali, mtengo umenewo udzawotchedwa.” Koma iwo sukuwotchedwa.

¹¹⁵ Oh, a—moto umangothirira iwo. Iwo umangotipatsa ife chiyembekezo chatsopano. Iwo kokha—iwo umangolimbikitsa iwo; yesero lililonse, kuyesedwa. Nthawi iliyonse imene mphepo iwomba mtengo ndi kuwukankhira iwo mmbuyo ndi mtsogolo, ndi mmbuyo ndi mtsogolo, iyo imangomasula mizu kuti ikhoze kuzama ndi kukagwira bwino. Nthawi iliyonse matenda akakantha nyumba yanu, nthawi iliyonse mayesero akakantha pakhomu panu, nthawi iliyonse oyandikana nanu akamayankhula zoyipa za inu, zimangokugwedezeni inu, kukumasulani inu, kuti potero inu mukhoze kufika pansu ndi kukagwira bwino pa Thanthwe Lamuyaya la Mawu osasunthika a Mulungu. Umo ndi momwe Mulungu amachitira izo. Iye amatumiza mayesero amenewo kuti akakuyeseni inu ndi kukakutsimikizirani inu, kudzakugwedezeni inu ndi kudzakupatsani inu kugwira kwatsopano.

¹¹⁶ Ndiye ife tikupeza kuti, pamene iye anachita zonsezo, otsutsa anayima pafupi ndipo anati, “Izo sizingagwire ntchito.” Koma chiyani? Mmisiriyo ankadziwa kuti mlatho wake ugwira. Iye ankadziwa kuti iwo ukanadzatero, chifukwa iwo ukanadzayesedwa.

¹¹⁷ Ndi chifukwa chake Mulungu anati, “Ine ndidzakhala ndi Mpingo wopanda banga kapena khwinya.” Amen. Iye anali atadutsa kupyola mmayesero. Ndipo mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu amayenera ayasedwe.

¹¹⁸ Pa tsiku lalikulu la chikumbutso ilo, pamene iwo ankapita, pamene mbali ziwiri zonse zinawuyambapo kuchokera kumbali ziwiri zonse, pamene iwo anakumana pakati pa gombe, munthu yemwe anamanga iwo, iye anati, “Ine sindimufunsa munthu aliyense.”

119 Amisiri onse atayima mozungulira, anati, “Kunjenjemera kulikonse kukangogunda mlatho umenewo, iwo udzangopita molunjika pansi. Iwo ukhala wowopsya.” Palibe kampani ya inshuransi yomwe ingamupatse iye inshuransi pa zimenezo.

120 Iye sankasowa inshuranse iliyonse. Iye anati, “Mlatho wanga ukhazikika.” Iye anali ndi chidaliro. Tsopano, iye ayenera awuyese iwo, chifukwa mbiri yake ili pachiwopsyezo. Ndithudi, iyo ili. Ndipo ngati iwo ukhazikika, icho chidzakhala chikumbutso.

121 Ndi chifukwa chake ine ndikudziwa kuti chipulumutso, cha Mulungu, cha nthawi zakale chija chokhudza mtima chidzakhazikika: mbiri ya Khristu ili pamenepo. Iye sadzatipatsa ife chinachake choti timangirepo Mpingo, osati zamulungu zopangidwa ndi munthu, osati pa chokuchitikira china cha ku sukulu, kapena kumanga seminare ina monga iwo ankafunira kuteru, mmawa uno, kuti awaphunzitse alaliki. Mlaliki weniweni amachokera ku seminare ya chisomo cha Mulungu, maitanidwe a Mulungu, ndipo zimakhala zoyesedwa ndi nthawi. Uko nkulondola. Izo zidzagwiritsitsa. Mulungu ali nacho chidaliro mwa inu. Ife tiri nacho chidaliro mwa Iye. Mlatho udzatero . . . Wandakatulo wakale anati:

Nangula wanga wagwira mkati mwa
chotchinga;
Mu chimphepo champhamvu ndi chamkuntho
chirichonse,
Nangula wanga adzagwira mkati mwa
chotchinga.

122 Ife sitikudziwa chimene chagwira, koma Chinachake chikugwira. Uko nkulondola. Iye wazikika kutsidya uko mmalo othawirapo. Ndipo kuli chingwe cha chipulumutso chimene chimagwira mtima wa munthu, kuti munthu yemwe anayamba wabadwanso kachiwiri wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Adierekezi onse ochokera ku gehena sakanakhoza kumupangitsa iye kuti akayikire izo. Pali Chinachake chikugwira mkati mmenemo. Msiyeni iye agwedezeke! Msiyeni iye agwedezeke! Amen. Iye amagwira, nthawi iliyonse, chifukwa izo ziri mwa Khristu Yesu.

123 Ndiye munthu uyu anati, “Ine sindimfunsa aliyense, koma,” anati, “Ine ndipitako, ndekha.”

124 Ameya a mzindawo anachokapo ndipo anati, “Bambo, ine ndithudi ndiri ndi chidaliro ndi mlatho wanu.”

125 Iye anati, “Ngati inu muli ndi chidaliro ndi mlatho wangawu, nditsatireni ine. Chabwino, uyeseni iwo.”

126 Ameya anati, “Galimoto yanga idzakhala ikuyenda pamenepo mmawa winawake. Ine ndipita ndi inu.”

¹²⁷ Kampani ya njanji inaitanidwa ndipo inati, inayimba ndipo inati, “Bwana, ife tiri ndi chidaliro ndi mlatho wanu. Ife tidzakhala...”

¹²⁸ Anati, “Ngati inu muli ndi chidaliro ndi mlatho wanga, bweretsani masitima foro odzaza, mudzawakhazike iwo pa mlathopo. Ngati inu muli ndi chidaliro, nditsatireni ine. Ngati inu mukukhulupirira kuti iwo wayesedwa ndi kupimidwa, inu mukukhulupirira zimenezo, bwerani, mupite ndi ine.”

¹²⁹ Ndipo anthu ambiri anamulembera iye makalata, kuti awone kulimba mtima kwake. Ndicho chimene anthu amayang’anapo ndi amuna olimba mtima, osati chinachake chawedewede pang’ono.

¹³⁰ Ngati inu mukuganiza kuti zikhoza kukuyenderani, chifukwa mumapita ku tchalitchi ndipo mumanena “ameni” kamodzi pakanthawi, ndi kufuula pang’ono, kulemba dzina lanu pa bukhu, ndi kubwererako ndi kumakakhala monga mdierekezi, ntchito zanu zomwe zimatsimikizira chimene inu muli. Khalidwe lanu latsimikizira zimenezo. Koma Mulungu...

¹³¹ Dziko likufuna kuwawona amuna amene ali olimba mtima, winawake wolimba mtima, yemwe angaime pamenepo, monga chikumbutso cha chisomo chopulumutsa cha Yesu Khristu. Uko nkulondola.

¹³² Tsiku limene mlathowo unayamba, ena onse anabwerera, anati, “Konzekerani. Bweretsani makamera anu,” iwo onse, atolankhani anati, “chifukwa mlatho umenewo ugwa.”

¹³³ Mnyamata ameneyo anayenda nkudzatulukira pa mlatho umenewo, anadzaimika galimoto yake pamenepo, anayang’ana mmbuyo pansi, iye anadzawona masitima amenewo onse atafola, iye anawawona ameya pamenepo akumubaibitsa iye. Iye anayang’ana ndipo iye anawona makumi a zikwi za oyenda pansi atayima kumbuyo uko, atakonzeka kuti agube naye iye. Anati, “Bandi iyambe kuimba.” M’bale, pamene mabandi anayamba kuimba, malikhweru anayamba kulira, zitoliro zinayamba kumamveka, ine ndikutanthauza kuti panali kugwedezeka kowopysa kukuchitika. Koma iye anayenda akuwoloka mlathowo, ndipo iwo sunasunthe nkomwe. Chifukwa chiyani? Iye anakhala patsogolo, chifukwa, ngati iwo ukanati ugwe, iye apite nawo iwo.

¹³⁴ Ndipo Yesu Khristu anabwera kuchokera Kumwamba, Ulemelero; kuchokera ku Ulemelero, pansi pano, kuti adzamange Mpingo. Ndipo zipangizo zimene Iye akuziika Mmenemo, ndi zipangizo zoyesedwa ndi nthawi. Inu mukhoza kubwera ku guwa ndi kudzapanga kuvomereza, koma pamene Iye apeza mabowo ophulika ndi china chirichonse, onani, dziko—dziko laphulitsa mphutsi mwa inu, ndi zina zotero, inu simungakhoze kuima nazo. Iye amangokuponyerani inu kumbali imodzi. Mulungu akufuna Mpingo woyesedwa ndi

nthawi; osati winawake amene ali Mkhristu lero ndi wobwerera mmbuyo mawa, mkati ndi kunja, ndi mmwamba ndi pansi. Iye sangakhoze kukuikani inu paliponse.

¹³⁵ Koma Iye ali nawo Mpingo umene wayesedwa, unadutsa mmayesero, unatayapo, unadutsa mmatenda, unadutsa mu chisoni, unadutsa mu imfa, ndipo komabe nkumaima ndi umboni. Ndiye munthu ameneyo, inde, ndiye munthu yemwe Iye akumuyembekezera. Ine sindikusamala ngati ndiwe wopemphetsa. Ine sindikusamala ngati ndiwe wopemphapempha. Ine sindikusamala ngati ndiwe wotoleza zotaya. Chirichonse chimene iwe uli, Mulungu amaika zayesedwako kwa inu. Iye akuyembekezera zida zomwe zayesedwa ndi nthawi. Ine ndikukhulupirira, limodzi la masiku awa pamene Mpingo waukulu uwo. . .

¹³⁶ Pamene, sayansi ikuti, “Zingatheke bwanji? Mphamvu yokokera pansi imakugwirirani inu ku dziko lapansi.”

¹³⁷ Tsopano ine ndikumverera mwachipembedzo. Ndiloleni ine ndikuuzeni inu. Mpingo woyesedwa ndi nthawi umenewo udzakhalapo tsiku lina. Pakhoza kukhala theka la iwo akugona mu fumbi lapansi. Ine sindikudziwa kumene iwo ali, koma Mulungu ali nazo zipangizo Zake zonse zinayesedwa. Tsiku lina Iye akubwera kudzatsogolera patsogolo: “Ndisatireni Ine!” Kudutsa kupyola mumlengalenga ndi mmiyamba, ndi mmayiko ndi mmayiko, kukalowa mu Kukhalapo kwa Mulungu Wamphamvuzonse Iye adzapita, ndi Mpingo woyesedwa ndi nthawi. Ndicho chikumbutso kwa chisomo Chake; ndicho chikumbutso chimene Mulungu amamupatsa Iye.

¹³⁸ “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Ndipo munthu aliyense amene abwera kwa Khristu ndi mphatso yachikondi yochokera kwa Mulungu, ndipo Khristu amamuyesa iye. Ndipo ngati iye apirira ndi kuyesedwako, Iye amamuika iye pa mlatho, amamumangirira iye pansi, amamupatsa iye udindo, ndipo amamukhazika iye pamenepo, akudziwa kuti iye adzagwira mpaka kumathero a njira. Amen. Zida zoyesedwa ndi nthawi!

¹³⁹ “Pa Thanthwe ili,” osati pa thanthwe lina la kutentheka, osati pa gulu la kutengeka, osati pa gulu la fioloje ya mpingo, osati pa chipembedzo china. Koma, “Pa Thanthwe lolimba ili,” Mawu a Khristu, “Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze konse kuwugonjetsa Iwo.” Iwo udzakhalapo pamenepo.

¹⁴⁰ Ichu chidzakhala chikumbutso cha chisomo Chake, mu kukhalapo kwa Angelo. Pamene Angelo anamufunsa Iye, tsiku lina, “Nchifukwa chiyani Inu mukupita kudziko lapansi?” Iye adzabwerera ndi kudzaupereka Mpingo umenewo wopanda chilema, wopanda banga, wopanda khwinya. Ndi zimenezo zidazo. Ndi chimenecho chinthucho. Mbiri yake. Iye ayenera

kuchita zimenezo. Womanga mlatho uja ankayenera kumanga mlathowo; iye ayenera kuchita zimenezo, kapena ayipitsa mbiri yake. Khristu adzakhala nawo Mpingo, ndipo Iye ayenera kuchita zimenezo. Chifukwa, Iye anabwera ku dziko lapansi ndipo anadzasandulika thupi, ndipo anadzakhala pakati pathu; ndipo anakhala tchimo, kuti ife tidzakhoze kukhala chirungamo. Iye anadzakhala ife, kuti ife, mwa chisomo Chake, tidzakhoze kukhala Iye. Iye anabwera kuti adzatenge malo athu, monga wochimwa; kutilola ife kukhala ndi malo Ake, monga ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, mu Kukhalapo kwa Ufumu Wake. Ndi chisomo bwanji cha Mulungu!

¹⁴¹ Ife tinganene bwanji, “Mawu amenewo si olondola”? Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu amenewo sadzapita konse.

¹⁴² Mnyamata wamng’ono wakhungu Wachimwenye, mausiku angapo apitawo, wakhungu kuyambira ali usinkhu wa zitatu—masabata atatu kapena foro, analandira kupenya kwake, mwachizolowezi, ndipo anachoka pa nsanja. Chinali chiyani chimenecho? Icho chinali chikumbutso choyesedwa ndi nthawi cha Mphamvu ndi chisomo cha Yesu Khristu. Lidalitsike Dzina Lake loyera!

¹⁴³ Kuyesedwa ndi nthawi! Mayesero, zovuta, zimagwedeza, ndi kukoka, ndi zoti zingopeza kumenya mwa inu, kuti awone ngati chiripo chirichonse pamenepo. Ndi Mulungu akukugwedezani inu ndi kukuyesani inu.

¹⁴⁴ Nthawi ina kale, Kaisara Augusta wamkulu, itatha nkondo yaikulu yotchuka, ndipo anapambana chigonjetso chachikulu, iye. . . iwo anali oti akukamupatsa iye chikondwerero ku Roma. Ndipo iye anati kwa iwo, “Ine ndikufuna mwamuna wina kuti akwere, mwamuna wina woyenera, kuti akwere pambali panga pamene ine ndikuchita izi.” Anati, “Ine ndikufuna mwamuna wina kuti agawane nane madalitso awa.” Ndipo zonse. . . Iwo unadutsa m’misasa. Atsogoleri onse anakonza nthenga zawo, ndipo anapukuta malupanga awo, ndipo anawalitsa zida zawo kwenikweni, ndi chirichonse, ndipo amaphunzira kuyima mowongoka, ndi malonje ena kwa mfumu yawo, ndi zina zotero.

¹⁴⁵ Ndipo aliyense anayenda chokwera, zida zawo zazikulu patsogolo pa iye, pamene iye anali atakhala pamenepo pa mpandowachifumu wake, akuyang’ana. Ndipo pamenepo panadzabwera, mdindo ali ndi nthenga yake yaikulu, yabwino, basi nthenga chabe, anayima ndipo anapanga sawasha yake. Kaisara anapukusa mutu wake; iye anachokapo. Wina anabwerapo, anadzapanga sawasha yake. Kaisara anapukusa mutu wake; ndipo iye anachokapo. Nthawi ndi nthawi, msirikali pambuyo pa msirikali.

¹⁴⁶ Potsiriza, mmusi momwe motsatira mzere, kunabwera munthu woyenda pansu. Iye analibe chishango choti

apukute, komanso analibe nthenga kuti adulire. Koma iye anayenda pamaso pa Kaisara. Iye sankadziwa nkomwe momwe angapangire sawasha yamtundu woyenera, koma iye anangoweramitsa mutu wake nachokapo.

¹⁴⁷ Kaisara anati, “Yembekeza miniti. Ndiwe ndani? Bwerera kuno.” Iye anayenda kupita pamenepo. Iye anayang’ana pa iye. Pali zipsyera pa nkhope yake, ndi mokhapidwa, ndi wosawoneka bwino, ndi wolumala. Anati, “Zipsyera zimenezo unazitengera kuti?”

Iye anati, “Uko ku nkondo, kumenyera mbuye wanga, Kaisara.”

¹⁴⁸ Anati, “Kwera pano ndipo udzakhale pambali panga. Ndiwe amene wayesedwa ndipo watsimikiziridwa.”

¹⁴⁹ M’bale, ino si nthawi yochepetsa nthenga, si masiku a maphunziro. Ndi nthawi yoyesera ndi nthawi. Ndi nthawi imene Mulungu akuwuyesa Mpingo Wake kuti apeze zipsyera za nkondo ya mayesero amphamvu, ndi ndewu, ndi nkondo. Ameneyo ndi amene adzakwere pambali Pake.

¹⁵⁰ Momwe Elisha anayesedwera ndi kutsimikiziridwa, iye asanavale mkanjo wa mneneri! Momwe Elisha anaponyera mwinjiro umenewo paphewa pake! Momwe iye ayenera kuti anali munthu woyenera! Elisha anamuyang’ana iye m’munda mmenemo, pamene iye anali kulima. Mulungu anati, “Mwamuna wake ndi ameneyo. Mwamuna wake ndi ameneyo yemwe akhoza kuvala chovala chimenecho. Mwamuna wake ndi ameneyo yemwe akhoza kuvala mwinjiro umenewo. Iye akhoza kutenga malo ako.”

¹⁵¹ Lidalitsike Dzina la Ambuye! Momwe diso Lake lopenyazonse likuyendayenda padziko lapansi, kuyesetsa kuti amupeze munthu wina yemwe ati adzavale mwinjiro umene Iye ankawukamba. “Kodi inu mukhoza kumwera chikho chimene ine ndikumwera? Kodi inu mungakhoze kubatizidwa ndi ubatizo umene ine ndiri? Inu mungathe,” Iye ananena kwa izo.

¹⁵² Chotero, ife, lero, monga Mpingo, inu muyenera kuvala mwinjiro wa Khristu; zida zonse za Khristu, chishango chonse ndi chikopa, ndi zida, kuti tidzakhoze kuima opanda chilema pa Tsiku limenero. Iye akufunafuna zikumbutso zoyesedwa ndi nthawi, pamene Iye angakhoze kunena kuti, “Ndi ameneyo wantchito Wanga. Ine ndamuyesa iye. Ine ndamuyesa iye. Ine ndamuyesa iye, monga Yobu. Iye akutsimikizirabe handiredi pa handiredi.” Mulungu atichitire ife chifundo, kuti tizikhoza kumutenga Mulungu pa Mawu Ake, ndi kukhala zikumbutso zoyesedwa ndi nthawi.

Tiyeni ife tipemphere.

¹⁵³ Atate Wodala, ife tikukuthokozani Inu, Mulungu Woyera Kwambiri, kuchokera mu kuya komwe kwa mitima yathu,

chifukwa cha kuyesa ndi nthawi, yesero lirilonse. Ife sitikuwamvera iwo chisoni, Ambuye, koma ndife oyamikira kuti chisomo Chanu chinali chokwanira kuti chitithandizire ife kudutsa mu nthawi zazikulu izi za mayesero.

¹⁵⁴ Monga bamboyo, usikuuno, momwe zinawasangalatsira omvetsera, pamene iye anatchula, *Chisomo Chodabwitsa*, ndipo pamene ife tinafika ku ndime inayakeyo!

Kudutsa mu zowopsya zambiri, zovutikira, ndi misampha,
ine ndabwera kale;
Chinali chisomo chomwe chandibweretsa ine wotetezeka mpaka pano,
Ndi chisomo chimene chidzandipititse ine patsogolo.

¹⁵⁵ Oh, izo zinakondoweza mitima ya anthu! Ife tikukhulupirira kuti izo zimapola ndi Uthenga usikuuno, kuti kunali kuyesa kwa nthawi, podutsa mu zowopsya, zovutikira ndi misampha. Zinali zoti zimuthandizire Mkhristu, amene wadziyesa yekha tsopano ndipo wadziwa kuti ndi wokhulupirika, mwa chisomo cha Mulungu. Izo zinali zoti zibweretse manyazi kwa iwo amene amagwa, ndi zokwera ndi zotsika, ndipo samasamala, ndi moyo wotayirira. O Mulungu, alibe ngakhale chipsyera chankhondo choti asonyeze nkhoodoyo. Ife tikupemphera usikuuno, Ambuye, kuti Inu muwuyeretse Mpingo, ndi Magazi Anu amphamvu overa, ndipo mutsuke nkhonya zonse, ndi malo onse ofooka, ndi—ndi maulusi onse oyipa. Adutsitseninso iwo mmakina kachiwiri, ndi—ndipo muwapangenso iwo atsopano, Ambuye, ndi—ndi kuwapanga iwo kukhala zipangizo. O Atate Wamuyaya ndi wodala, imvani pemphero la wantchito Wanu.

Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa.

¹⁵⁶ Ngati pangakhale munthu woteroyo pano usikuuno, yemwe angamverere kuti Mulungu, mu nthawi yoyesa iyi, sanakupezeni inu wokhulupirika pa ntchito. Pamene mikangano ibwera, kapena kodi inu mumalumphira momwemo ndi kutenga nawo mbali? Pamene mikangano ibuka, pamene kusayanjanitsika, pamene mikangano mu mpingo ifika, kodi inu mumatenga mbali ndi mipingo ndi timagulu, ndi zina zotero monga choncho? Kodi inu mumamvetsera miseche mmisewu ndi mozungulira malowo? Ngati ndinu wolakwira zimenezo, inu mwaphwanyidwa ndi nkhonya za mdierekezi, tiyeni tibwerere ku ng'anjo, usikuuno, ndipo tikasungunulidwensu, ndipo tikatulukeko opanda zimenezo mwa ife. Timulole Mulungu atikonze ife ndipo atikonzekeretse ife Mlatho waukulu uwu wotenga Mkwatulo Wake. Ngati munthu woteroyo ali pano, ndipo angafune atakumbukiridwa!

¹⁵⁷ Inu mukuti, “M’bale Branham, ine ndingadziwe bwanji kuti chikumbutso chachisavundi ichi, Chamuyaya chidzayima?”


158 Ine ndikubwerezerani inu Mawu Ake, molingana ndi Yohane 5:24. “Iye amene amva Mawu Anga.” (Osati “Amapita ku sukulu Yanga.”) “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo; koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

159 Kodi inu mukukhoza kuwamva Mawu Ake akukuitanani inu, usikuuno? Ngati inu mungathe, ndipo mufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero, kodi inu mungakweze dzanja lanu. Mukuti, “M’bale Branham, mungondipempherera ine. Ine ndikufuna kuti ndikhale mtundu woyenera wa chipangizo, kuti pamene Khristu azidzawubweretsa Mpingo Wake, kuti ine sindidzakhala . . .” Mulungu akudalitseni inu, bwana. “Ine ndisadzakhale wogwedezeka nazo izo, Iye adzandiyika ine mu Mpingo momwe.” Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. “Ine ndikufuna kukhala . . .” Mulungu akudalitseni inu, m’bale. “Ine ndikufuna kukhala mtundu woyenera wa chipangizo.” Mulungu akudalitse iwe, wamng’ono kumbuyo uko. Mulungu akudalitseni inu kuno, m’bale wanga wokonedwa. “Ine ndikufuna ndidzapezeke ndiri chipangizo chenicheni. Ine ndikufuna ndidzakhale wokhoza kupereka umboni wa chiyembekezo chimene chiri mwa ine; chiyembekezo!” Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndizo zabwino. Uko nkulondola.

“Kodi izo zikuchita chiyani, M’bale Branham, pokweza mmwamba manja anga?”

160 Inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo. Ndi zimene inu mukuchita. Inu mukuswa lamulo lililonse la mphamvu yokokera pansu, pomwe apo. Mwaona, ngati inu mukanangokhala chithunzi chitakhala pamenepo, inu simukanakhoza konse kukweza dzanja lanu. Inu simukanakhoza kuchita zimenezo. Koma izo zikusonyeza kuti muli mzimu mwa inu, mzimu, ndipo mzimu umenewo wamva Mzimu wa Mulungu ukuyankhula kwa inu. Ndipo mzimu uwo umene uli mkati mwanu wapanga chigamulo, chotero izo zimatsutsa sayansi. Izo zimatsutsa mphamvu yokokera pansu. Izo zimakwera mmwamba, kusonyezera kuti muli mzimu mwa inu, mukhoza kukweza dzanja lanu. Ngati inu mukanakhala wakufa, inu simukanakhoza kuchita zimenezo, koma inu mwabwera ku Moyo. Chinachake chachitika.

161 Ngati mukanakhala wakufa mu tchimo ndi kulakwa, Mulungu sangakhoze kuyankhulanso ndi inu, dzanja lanu likanakhala pansu. Ngati inu simuli akufa mu tchimo ndi nkulakwa, ndipo Mulungu akhoza kuyankhula ndi inu, ndipo inu nkulandira Moyo, inu mudzakweza dzanja lanu. Mwaona, zikusonyeza kuti Moyo wapanga chigamulo, inu mwamulandira Khristu. “Inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo,” ngati inu mukutanthauza zimenezo.

¹⁶² Tanthauzani izo tsopano, pamene inu mukukweza dzanja lanu. Nenani, “Mulungu, mundichitire ine chifundo, ndipangeni ine chimene ndiyenera kukhala. Ndipo ine ndidzakutumikirani Inu moyo wanga wonse. Ine ndikufuna ndidzapezeke wokonzeka tsiku limenero.” Mdalitso pa inu, m’bale wanga wokondedwa kumbuyo uko. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, pamenepo m’ba-...Mulungu akhale nanu. Mulungu akudalitseni inu, wokondedwa. Chabwino, winawake. Mulungu akudalitseni inu apa, M’bale Roy, ndipo Ambuye akhale nanu. Inde. “Ambuye, ndipezeni ine woyenera. Ndipezeni ine woyenera.” Mulungu akudalitseni inu, m’bale wanga kumbuyo komwe. Ndithudi, Mulungu akukuwonani inu. Khalani okondwa. Winanso akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero pakali pano? “Ndipangeni ine . . .” Chabwino. Tiyeni ife . . . 

ZIKUMBUTSO ZOYESEDWA NDI NTHAWI ZA MULUNGU CHA57-0818
(Time-Tested Memorials Of God)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Ogasiti 18, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org